


TSIKU LA ANAKUBALA

 ...Kachisi, liri pemphero langa. Ine ndiri wokondwa ndithu mmawa uno, kuwona kuyima mwauzimu kwa Kachisi uyu, ndi momwe kuti, chizindikiro kunjira uko, iwo akonzeka tsopano kumanga tchalitchi chatsopano. Ine ndikuganiza icho chikufunika. Ndi kuwona zotsatira... ngati Ambuye Yesu achedwa, ife tikadzakhala titapita, iwo adzakhala... ana athu adzayenera kukhala ndi malo opitako ku tchalitchi. Ndipo ife tikufuna kuti “modzipereka kukanganira pa Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera mtima.” Ganizani icho ndicho chinthu chabwino.

² Ndipo pamene ine ndinali kulowa kumene, mphindi zingapo zapitazi, kuwonjezera ndi mawumboni ambiri amene aperekedwa kale okhudza za machiritso, a misonkhano ingapo yapitayo, ku Kachisi kuno. Iwo akungowunjikana pamodzi mosalekeza, a machiritso, machiritso ozizwitsa opambana.

³ Ine ndinamusiya mkazi wanga kunjira, tsopano pomwepa, ndi ana pa—khomo; ndipo pamenepo panali mlongo, wakhala pomwe pano tsopano, kungokomedwa chotero mpaka iye amalira, za chozizwitsa chachikulu chomwe chinachitika pa mzukulu wake wamng’ono wamwamuna, komwe uko, ine ndikulingalira, mu Chattanooga. Akazi a Nash, pano, mzukulu wanu wamng’ono wamwamuna amasautsika ndi chomusautsa, ndipo msonkhano wathawo pano, Ambuye Yesu, ine ndikuganiza, anachitchula icho, ndi kuti, “PAKUTI ATERO AMBUYE, kuti, izo zatha. Ndipo iye akhala bwino.” Ndipo kamwanako kali bwinobwino mwangwiwo ndi ubwino, kungokhala bwino momwe iye angakhalire.

Ndipo ziri—ziri zokoma kumva maumboni amenewo.

⁴ Ndiyeno mnyamata wamng’ono, amene alinso pompano, anapempha pemphero kwa Akazi a Stotts, amene angochitidwa opareshoni kumene. Ndipo chowakondweretsa chawo; onani, ngati palibe amene akufuna ife kuti tiwapempherere iwo, chifukwa chawo...izo zimawonetsera, pokha pamene inu mukuyesera, anthu kufuna iwe kuti uwapempherere iwo, iwo...kukondweretsa, inu mukuona. Nthawi zina zimafika poyipa kwambiri, mpaka...osati kuyipa, koma ochuluka kwambiri, koti iwe umangothawira kunjira kwinkwake ndi kukabisa mutu wako kutali, ndi kubisala kwa kanthawi kakang’ono, kuti ukhale moyo. Koma, ine—ine ndiri wokondwa iwo amachita zimenezo. Musaganizire konse kuti ine sindikonda kuwawona iwo, chifukwa ngati iwo...ngati pakanakhala palibe wina wofuna kuti ine ndiwapempherere iwo, utumiki wanga ukanakhala kuti? Mwaona? Mwaona?

⁵ Koma nthawi zina pamene inu munena, “M’bale Branham, ine sindikumvetsa pamene anthu akuyitana motero, ndipo—ndipo inu muzembera kwinakwake.” Ine ndiyenera kuchita zimenezo kuti ndikhale moyo, kuti upempherere anthu. Inu simukungo... Izi siziri—siziri kumalo amodzi wokha, kuno. Ziri konsekonse mu dziko. Inu mukuwona? Ndipo—ndipo ndi zovuta ndithu. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu mukumvetsa zimenezo.

⁶ O, ndi bwino kwambiri kukhala Mkristu! Ine sindikudziwa chomwe ine ndikanamachita ngati sizikanakhala kwa Khristu, ndipo kotero... ndi kukhala woyanjana ndi Akhristu, kuti, anthu a Chikhulupiriro chofanana chopambana, amene amakhulupirira mwa Mulungu ndipo akumudalira Iye; ndi kukhulupirira kuti tsiku lina la ulemhero ife tidzakhala titathana nayo nkondo yonse, ndi kukhala ndi chigonjetso, ndi kuyima owomboledwa mu mawonekedwe Ake, ku dera linalo.

⁷ Ndiyeno ine ndikufuna kungopanga cholengeza mwachidule, kuti, mukubwera kwa Kachisi, ndi zina zotero, ine... ife tikupanga kukonzanso kwa maziko athu, makamaka gawo langa la kulengeza. Kuchokera konseko kupyola mu misonkhano, kuchokera pamene ine ndinayamba mu izi, pa mbali ya kufalitsa uthenga, zaka zambiri zapitazo, mmalo moyambitsa maziko, kukhala ndi gulu lina la anthu, ine ndinangogwiritsa ntchito gulu limene ine ndimadziwana nalo; ndipo kuchokera... ndipo ndinapanga maziko, kuti misonkhano yanga yonse izidzakhoza kuchitidwa mu dzina la Branham Tabernacle. Ndipo ilo likhoza kumadzagwiritsidwa ntchito ku Union National Bank mu New Albany, monga kumene ndalama zizidzalipidwa—kulipidwa kupyolera mwa ilo, kuti izo zisamadzakhale ndi msonkho. Ngati ine sindikanatero, ndalama zonse zolandiridwa zikanamalipiritsidwa msonkho kwa ineyo, ngati ine ndikanati ndisamagwiritse ntchito Branham Tabernacle ngati maziko.

⁸ Ambiri a inu mwandimvapo ine ndikulengeza zimenezo, nthawi ndi nthawi. Ine ndiyenera kuchita zimenezo, ndi ku... pofuna kuti uchite zimenezo. Ndipo kenako—kenako ife tikukhazikitsa maziko atsopano tsofano. Ndipo ife tikanakonda ambiri onse amene akudziwa kuti ine... Ndi angati anandimvapo ine ndikulengeza zimenezo, kuti mphatso zonse, ine ndimagwira ntchito kupyolera mu Branham Tabernacle? Tangokwezani manja anu, onse... Zedi, nonse a inu. Ndi onse.

⁹ Ndipo kotero pamene ulaliki utha, ngati inu mufuna, ine ndiri ndi cholankhula chaching’ono pamenepo, kotero kuti inu, ngati inu mungasayinire zimenezo pamene mukutuluka kunjani. M’bale Roy Roberson adzakhala nazo izo kumbuyoko.

¹⁰ Chifukwa, ife tikhazikitsa maziko ena, chinthu chomwecho, chabe...koma maziko ena, kuti ndalama zathu zonse ndi zinthu, zimene zatengedwa mu misonkhano, kutetezera kuti zisakhomeredwe msonkho, zidzakhala...zayikidwa, monga nthawi zonse, mu Union National Bank, kuti zizigwiritsidwa ntchito kudzera mu Kachisi, mmalo mokhala—mazi-...maziko ena. Chifukwa, awa ndi maziko kale, mu dzina la Branham Tabernacle, inu mukuwona. Ndipo kotero pali Branham *pano* ndi Branham *uko*, ndipo monga izi, ndi maziko osiyana amene sakuchita bwino kwambiri.

¹¹ M'bale Roberson adzasamalira za zimenezo, inu amene mudzafune, pamene ife tikutuluka kunjja. Ife tidzayamikira zimenezo.

¹² Tsopano, mmawa uno, ife tisanalowe mu ulaliki, ine ndikufuna ndinene, Ambuye akalola, kuti ine ndiyesera kubwera kachiwiri usiku uno. Ine ndikudana ndi kutenga misonkhano yonse iwiri kwa M'bale Neville, koma iye wandipempha ine mokoma mtima kuti ndilankhulenso usiku uno. Ndipo ngati Ambuye alola, ine ndikufuna kulankhula usiku uno pa mutu wa kufalitsa uthenga wa, wotchewa chotere: *Ameneyu Ndi Ndani?* Mwaona? *Ameneyu Ndi Ndani?*

¹³ Ndipo kotero mmawa uno, ine ndikufuna ku...Ine ndimaganzira za—za kulankhula mmawa uno pa phunziro la Tsiku La Anakubala. Ndipo ine ndikudziwa kuti madzulo ano ndi mmawa wonse wadzazidwa ndi madongosolo a Tsiku La Anakubala. Kotero ine ndinaganiza ine ndikhala ngati kuphatikiza chinachake, chifukwa ife tikufuna tipempherere odwala ukangotha ulaliki uwu, ndipo monga mwa chizolowezi.

¹⁴ Ife tikukhulupirira kuti Mulungu ali mchiritsi, ndipo Iye amachiza odwala ndi ovutika. Ndipo ine ndikudziwa Iye amachita zimenezo. Ndipo ndi zopitirira kalikonse—kukayikira kulikonse, kuti, chifukwa pali mawumboni ambiri awunjikizana, kuti ife tidziwe zimenezo.

¹⁵ Dzulo ine ndimayang'ana mu thumba lomwe M'bale Gene ndi Leo amangolisunga, la mawumboni amene iwo anawatenga. Ndipo linali thumba lalikulu lapadera, machiritso ozizwitsa amene Ambuye awachitira anthu.

¹⁶ Ndipo ine ndinaganiza, ngati izo zingakhale motero, bwanji ngati ife titasunga chiwerengero cha zonse zimene zachitika? Ine ndinaganiza, mu Puerto Rico ndi Jamaica, mokha, chingathamangire zikwi khumi, kapena kuposapo, mawumboni apadera, a machiritso a Ambuye, omwe Iye anachita.

Tsopano ife tisanatsegule Bukhu, tiyeni tilankhule kwa Mlembi.

¹⁷ Ambuye, ife ndife oyamikira kwa Inu, kuti ziri, pamene ife tiweramitsa mitu yathu, ife timangochita chibwibwi ndi mawu oti tinene; pakuti ine sindimakhulupirira kuti zimakhala mu

milomo ya umunthu kuti awonetsere zokhudza za mu mtima wa mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena msungwana, amene anakhudzanapo ndi Inu. Kuti tiwonetsere kukukondani kwathu, za momwe ife tikukonderani Inu, ndi chimene Inu mutanthawuza kwa ife. Izi zatipatula ife ku tchimo, ndipo zinatipatula ife ku za mdziko. Ndipo izi zikutipatsa ife chinachake chimene chiri Chamuyaya ndi chodalitsa. Ndipo ife sitikanapeza mawu okwanira.

¹⁸ Monga zinalankhulidwapo ndi mwamuna wolemekezeka, masabata angapo apitawo, kuti iye amakhoza kulankhula mosalakwitsa mu zilankhulo zisanu ndi zinayi zosiyana, kugwiritsa malo ake ndi mlangizi kwa Puzidenti wathu wokondeka, Dwight Eisenhower. Ndipo ngakhale anali wokhoza kulankhula zilankhulo zisanu ndi zinayi, mosalakwitsa; iye anati, pamene iye analandira Mzimu Woyera, iye anayesa zonse zisanu ndi zinayi, ndipo panalibe mawu amene iye akanakhoza kuwapeza, palibe chimene iye akanakhoza kufotokozerana, ndipo kotero Inu munamupatsa iye chilankhulo chatsopano kuti afotokozerana ndi kukuthokozerani Inu nacho. Ndipo ife tikukhudzidwa' mwa njira yomweyo, nafenso, Ambuye; kuti, pamene moyo utha, kuti mwinamwake ife tidzalankhula tonse palimodzi mu chilankhulo chosiyana, kotero ife tikhoza kufotokoza chimene ife tikuganiza za Inu.

¹⁹ Tsopano ife tikufuna kufunsa, Ambuye, kuti Inu mukhoze kudalitsa Kachisi uyu, m'busa wake, matrastii ake, madikoni ake, onse ochitira nawo palimodzi, anthu amene amadzacheza kuno, kulowa ndi kutuluka pa makomowa. Azipezeka nthawi zonse odzipereka, malo a mpumulo, kimene wofooka akhoza kudza mu makomo ake napeza mpumulo ndi mtendere kwa moyo wawo. Ndi kuti odwala akhoza kulowa mkhomo, natuluka ali abwino, chifukwa cha Kukhalapo kosalekeza kwa Mulungu Wamphamvuzonse Amene amakhala pansu pa denga lakeli.

²⁰ Ife tikufuna kufunsa, Ambuye, kuti mu dongosolo likudzali la . . . limene likukonzedwa tsopano, kuti Inu mukhoza kukumana ndi gulu loyang'anira ndi kukumana ndi onse. Ndipo ngati zikukukondweretsani Inu kuti pakhoze kukhala kupitirira kwa chikumbutso cha pemphero limene linapempheredwa mu dziwe lakaleli, ndi kamalo ka zomera, tsiku limodzi; kuti tsopano lasandulika nyumba ya kuunika, malo a mpumulo kwa ofooka, chifukwa cha yankho la pemphero lija.

²¹ Tsopano mutikhululukire ife pa chirichonse chimene ife tachichita, kapena kulankhula, kapena kulingalira, chimene chinali chosiyana ndi chifuniro Chanu chopambana; ndipo kumbukirani, Ambuye, icho sichinachokere mu mitima yathu. Ife mwina tikhoza kungofotokoza icho mu machitidwe athu kapena mwa milomo yathu. Koma, mofulumira, Inu munatimva ife. Pamene ife tinawona kuti tinalakwitsa, ife tinali ololera kuzirapa izo. Ndipo ife sitikufuna kuzisunga mu mitima yathu,

kusaweluzika, ndiye ife tikudziwa kuti Mulungu sadzayankha mapemphero athu; koma nthawizonse kuvomereza zolakwitsa zathu.

²² Ndipo ife tikufuna kupempha, Ambuye, kuti Inu mudalitse, m'mawa uno, konsekonse dziko lino, pamene likukondwerera tsiku ili la chikumbutso cha Tsiku La Anakubala. Koma ichi chisangokhala—tsiku la anakubala; tsiku lililonse lizikhala chotero.

²³ Mulungu, perekani mmawa uno, kuti amayi, akazi, amene asocherera kutali ndi Mulungu, kuti iwo adziwe chomwe ali mmawa uno, ndipo adzazindikire kuti mawu oti *mayi* amatanthauza, “iye amene waberekapo.” Azindikire iye kuti obadwawo, kuchokera mu chilumikizano chake ndi mwamuna wake, chakhala timiyala tating'ono topatulika timene Mulungu watiyikiza pansu pa chisamaliro chake. Ndiye, Mulungu adzamuwerengera iye udindo wolera ana amenewo. Ndipo monga Malemba anena, kuti, “Mkazi wabwino, ndi mayi, chimene iye ali, kuti ana ake adzamutcha iye wodala.”

²⁴ O Ambuye, pamene ife tikuwona tsiku ili, pamene iwo akupita kutali ndi Malemba, ndi kumachita ngati pafupifupi zirombo! Ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutipatse ife chitsitsimutso chachikale chimene chingawayitanire iwo kubwerera ku malo kumene iwo ayenera kukhala.

²⁵ Ambuye, ife sitingathe, mwanjira iliyonse, kuyiwala kukuthokozani Inu chifukwa cha amayi enieni, pakuti ife tikudziwa kuti ife tirinawo otero ali moyo lero; enieni, amayi owona. Mulungu, adalitseni iwo. Iwo ali chuma chopambana kwa ife, ndipo ife tikupemphera kuti Inu mupitirira kukhala nawo, Ambuye, ndipo iwo akhale moyo wokondwa ndi kuwona chipatso cha mimba yawo chikutumikira Mulungu.

²⁶ Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti iwo amene avala rozi loyera m'mawa uno, kapena duwa loyera, kunena kuti mayi wawo wapita kuseri kwa zochitika za lero izi; aloleni, Ambuye Mulungu, iwo apumule mu mtendere ndipo ntchito zawo ziwatsate iwo. Perekani ichi, Ambuye.

²⁷ Tsopano tengani Mawu Anu, Ambuye, ndipo lankhulani kwa anthu, ndi kuwapatsa iwo chithonhozo, pakuti icho ndiye chifukwa chake ife tasonkhanira pano; kuti timverere Kukhalapo Kwanu, kumva Mawu Anu, ndi kukhala odalitsidwa; ndi kuchoka pano kukakhala amuna ndi akazi abwino, anyamata ndi asungwana, koposa momwe ife tinaliri pamene ife timalowa. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwana wa Mulungu. Amen.

²⁸ Ine ndimakonda kuwerenga kwa Mawu Ake odalitsidwa. Kotero tsopano ife titembenuza, mmawa uno, mu Bukhu la Akorinto Woyamba, ndi kuwerenga mwa gawo la mutu 15, kuyambira ndi ndime ya 1.

Powonjezera, abale, ine ndikuwonetsera kwa inu uthenga umene ine ndinalalikira kwa inu, umenenso inu mwaulandira, ndi womwe inu mwayima mwa iwowo;

Umenenso inu mukupulumutsidwa nawo, ngati inu muwusunga mu chikumbumtima kuti ine ndinawulalikira kwa inu, pokhapokha ngati inu mwakhulupirira mwa chabe.

Pakuti ine ndinapereka kwa inu poyamba pa zonse zomwe inenso ndinalandira, momwe Khristu anafera machimo athu monga mwa malemba;

Ndi kuti iye anayikidwa mmanda, ndi kuti iye anawukanso tsiku lachitatu monga mwa malemba;

²⁹ Inu mukhoza kunena, “M’bale Branham, iyo ndi ndime yosazolowereka kani kwa uthenga wa Tsiku La Anakubala.” Chabwino, izo ndi zowona. Koma, inu mukudziwa, Mulungu ali wosazolowereka, ndipo Iye amachita zinthu mwa njira yosazolowereka.

³⁰ Ndipo ine ndikuganiza, malingaliro, a mayi. Ndipo ine ndiri nalo limodzi mmawa uno, mwa chisomo cha Mulungu, amene alipobe pansi pano ndi ife. Ndipo ine ndiri woyamika chifukwa cha mayi. Koma pokhala kuti ife tinayenera kukhala nawo, aponso, ulaliki wa machiritso, ndipo mosazindikira kuti ine ndibwereranso usiku uno, koma ine ndinaganiza kuti mwina ife tijambule chithunzi cha mtundu wina.

³¹ Mayi ali wopambana kwambiri. Inu mukudziwa, woyamba amene amakulandirani inu, mu moyo uno, ndi mayi wanu. Palibe wina angakugwiredi inu, chifukwa inu muli mmimba, ndipo iye amakunyumulani inu pansi pa mtima wake. Ndipo iye ali woyamba kukudziwani inu, ndipo woyamba ku, mu moyo uno, ku—kukunyumulani inu. Ndiye, pamene inu mwabadwa, iye ali mmodzi wa manja oyamba amene amakugwirani inu ndi kupukuta misonzi mmaso anu. Iye ndi woyamba kukusisitani inu ndi kukukondani inu, ndi kufungatira pa inu, mu moyo uno, ndiye mayi wanu. Tsopano, ine ndikuganiza kuti palibe kulemekeza kokwanira kumene tikanakhoza kupereka kwa mayi.

³² Mayi ali woyamba kukhala ndi mwana, ndipo iye ali udindo waukulu wa chomwe mwanayo adzakhale, maziko ake adzakhala momwe mayi wayambira naye mwana ameneyo pa njira imene iye adzayendapo. Mayi ali ndi udindo, kuchokera kwa Mulungu, kumuyika mwana ameneyo pa njira yoyenera. Ndipo ine ndikuganiza ndicho chifukwa chake anakubala ali ndi kagwiridwe kakang’ono kapadera.

³³ Ine ndikudziwa za mnyamata mu mzinda uno. Ine ndikuganiza mayi ake ali pano tsopano. Iye ndi wa pafupifupi msinkhu wangawu. Koma ine sindikunena izi kuti ndipweteke mayiwo; chifukwa choti iwo ali ndi zopweteke zokwanira,

monga anakubala onse. Koma mnyamatayo amamwa, ndipo iye amamwa kwambiri. Ndipo pamene iye aledzera kwenikweni, iye amabwera kunyumba ndi kudumphira mu bedi ndi mayi ake nayika manja ake mowakumbatira iwo. Ndipo iye ali ndi zidzukululu. Koma pali chinachake pa kusisita kwa mayi, kumene kukuwoneka kukutenga—malo osiyana oposa china chirichonse chomwe chingagwire; umo ndi, mu moyo uno, kunena mwaumunthu.

³⁴ Inu mukudziwa, mwamuna monga Mose, iye... Ngati ine ndikanakhoza kuyamikira chirichonse kwa khalidwe lake, chinali chifukwa iye anali ndi mayi wotumidwa ndi Mulungu. Inu mukudziwa anali iye amene anapemphera, Yokebedi, ndipo iye anali atamuyembekezera mwana ameneyu. Ndipo pamene iye anabadwa, iye anali yemwe ankamufungatira mwanayo, ndi kumuyangata iye ndi kumumangira likasa namuyika iye mkati mwa mnjeza, pamenepo mtima wake wosauka ukusweka. Kamwana kake kokhako, ndipo iko kanali—kamwana kowoneka bwino kwambiri kamene kanalipo mu dziko lonse. Ndipo momwe mayi amakondera mwana aliyense! Koma kukawona kamwana kapadera aka.

³⁵ Ndiyeno, mu mtima wake, iye anadziwa kuti iye anabadwira cholinga, ndipo kenako kumutenga iye ndi kukamuyika iye mu chisa chomwe cha ng'ona, uko mu mtsinje. Mwa chikhulupiriro iye anachita zimenezo, podziwa kuti Mulungu anali wokhoza kumusamalira iye; ndiko kukamba mwachidule za chikondi cha mayi, ndi kachitidwe ka khalidwe la chikhulupiriro chake. Pakuti chikhulupiriro sichimadziyika chokha pa michenga yosunthika ya chimene icho chingapenye; chikhulupiriro chimapuma mokhazikika pa thanthwe losasunthika la Mawu Amuyaya a Mulungu. "Pakuti mwa chikhulupiriro," atero Malemba, "iye anachita zimenezi."

³⁶ Ndipo chikhulupiriro chikhoza kutenga kuyima kwake pa thanthwe, limene mafunde akumenya maziko ake, ndi kuyang'ana molunjika mu nkhope ya imfa ndi kudziwa kuti zidzakhala mwa kanthawi kochepe chabe, koma chikhulupiriro chikhoza kuyang'ana patsidya la nyanja kwa Iye amene anati, "Ine ndine chiwukitsiro ndi Moyo," ndi kulephera ngakhale kumva mafunde akudumphira.

³⁷ Uwo ndiwo mtundu wa chikhulupiriro chimene mayi a Mose anali nacho. Iwo anamuphunzitsa iye ndipo iwo anamulera iye mu nyumba yachifumu ya Farao, kumuphunzitsa iye kuti iye anabadwira cholinga, kuti Yehova anayankha pemphero lawo. Ndipo, iwo, iye sakanakhoza kukhala ndi mphunzitsi wina woposa. Icho ndi chimene chinathandiza kuwumba khalidwe lomwe Mose anali.

³⁸ Ine ndikukhulupirira anali Abraham Lincoln amene kamodzi analankhula chotere...

³⁹ Tsopano, ine sindine Democrat kapena Republican, ine chabe...ine ndine Mkhristu. Pakuti, ine ndikuganiza mbali imodzi siikanakhoza kunena chirichonse mosutsana ndi mbali ina; zonse ndi zosokonezeka. Koma, Abraham Lincoln, mwa kuganiza kwanga, anali mmodzi wa...ndipo anali mmodzi wa Atsogoleri opambana amene United States anakhala nawo; kuphatikizapo Washington, ndi ena otero.

⁴⁰ Pakuti, Abraham Lincoln anali ndi—ndi kuyamba koyipa. Iye anali wosawuka. Iye analibe maziko, pokamba za maphunziro, kapena—kapena chinachake chachikulu, kapena ndalama, kapena chinachake chomwe chikanakhoza kumuthandiza iye, monga Washington anachitira. Washington anali wotsiriza maphunziro ku koleji, ndipo iye—iye amadziwa; iye anali mwamuna wanzeru, mwamuna wopambana, poyamba pomwe. Koma Lincoln analeredwa mu kanyumba kamatabwa, ku nthaka zopambana za Kentucky, ndipo mopanda ulemerero; mu kanyumba ka matabwa kachikale, kamene kali monga chikumbutso kuno ku Louisville tsopano. Koma, pokhala mwamuna wopambana yemwe iye anali, ndipo anachita kuphunzira kulemba, pa nthaka yomwe iye ankali mapo, kuti abzale chimanga.

⁴¹ Koma ine mwina ndingapereke ichi kwa anthu aang'ono. Kodi inu mukudziwa Abraham Lincoln sanakhale nalo bukhu mu moyo wake, kufikira iye atatha zaka makumi awiri ndi chimodzi, kupatula Baibulo ndi bukhu la anthu ofera choonadi la Foxe. Onani, chimene inu muwerenga chimawumba khalidwe lomwe inu muli. Ndi zosadabwitsa ife tiri ndi gulu la osokonezeka lero; ti magazine ta nkhani zopeka, ndi tauve ndi tamkhutu, tayikidwa pamalo ogulitsira zowerenga. Iye anali ndi Baibulo ndi bukhu la ofera choonadi la Foxe. Yang'anani chomwe icho chinamupanga iye!

⁴² Koma pamaso pa zonsezo, tsiku lina iye analankhula chotere. Iye anati, “Ngati pakanakhala chinthu china chabwino chopezeka mwa ine, ndi chifukwa cha mayi wa umulungu,” amene anamulera iye kuti atumikire Ambuye.

⁴³ Inu mukuona, mwana amamvera kwa mayi wake; kagwiridwe kena kamene ali nako mayiyo, kamene mwana angakamvere. Pamene mwanayo wapweteka, iye amapita kwa mayi kukatonthozedwa asanafike kwa bambo. Chifukwa, iwo anali woyamba naye, inu mukudziwa. Ndipo pali mphatso zina zimene Mulungu amazipereka kwa mayi, kuti zikhale motero; ine ndikutanthawuza mayi weniweni. Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti amayi ali olemekizeka ndi aumulungu.

⁴⁴ Koma ine ndikukhulupirira, monga Tsiku La Anakubala, monga ili, ndi khwekhwe, kupanga ndalama zambiri pogulitsa maluwa ndi zina. Koma tsiku la anakubala liyenera kukhala tsiku lililonse. Osati kuwatumizira iwo mulu wa maluwa pa

Tsiku La Anakubala, koma kuwakonda iwo ndi kuwasamalira iwo masiku mazana atatu makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zisanu ndi usiku, mu chaka chonse. Koma, indedi, malonda a mdziko agwira kwambiri mu zinthu monga izi, ndipo izo—izo—izo zimamufwifwitsa mayi.

“O, chabwino, Tsiku La Anakubala lapitali ine ndinawatimizira iwo mulu wa maluwa.”

⁴⁵ Iwo akhoza kuyamikira, kochulukirapo ndithu, mukanangokhala pansi ndi kulankhula nawo pang’ono pokha, kuwalemba iwo kalata, kuwasisita iwo pa phewa, kuwapsyopsyona iwo pa tsaya, kuwauza iwo kuti inu mumawakonda iwo. Zingafike patali koposa maluwa onse amene inu mukanakhoza kugula kuchokera kwa ogulitsa maluwa. Izo nzowona.

⁴⁶ Ine ndikukhulupirira izi zinali mu Malamulo Khumi, malemu Cecil DeMille, amene analemba ndi kuyika pa kanema imodzi mwa mbambande za mdziko la kanema. Ndipo iyo isanayikidwe poyera, kapena kutulutsidwa, Cecil DeMille anayitana Oral Roberts ndi Demos Shakarian, ndi gulu la azitumiki a Full Gospel, anawatengera iwo kowonetsera kwake nawawonetsa maora anayi a Malamulo Khumi, ndipo anawafunsa iwo maganizo awo pa iyo. Mulungu apumise moyo wake wodzipereka!

⁴⁷ Ndipo pamene ine ndinayiwona iyo, ndinali kuyang’ana pa iyo, ndipo kandemanga kanakanirira mwa ine nthawi zonse. Ngati ambiri a inu amene munayiwona iyo, panali pamene mwana wamkazi wa Farao... Mose atazindikira kuti iye anali—Myuda, ndipo iye anasankha kupita kumakakhala ndi anthu ake. Ndipo apo panakhala yemwe anali mayi wake wokongola, atafwifwa, ali ndi tsitsi lake la imvi ndi nkhope yake yamakwinya, atakhala mu m’pando wakale, mayi weniweni. Ndipo mwana wamkazi wa Farao analowamo. Ndipo iye anati, “Ndine mwana wa yani; mulimonse?”

⁴⁸ Ndipo pamene zinabweretseredwa poyera, kuti Yokobedi anali mayi wake weniweni. Mwana wamkazi wa Farao, ndi penti yake ndi zina zotero, ndipo zonse zitakonzedwa; iye anati, “Koma, tayang’anani! Iye mwina ndi mwana wanu, koma,” iye anati, “Ine ndinamupatsa iye chuma ndi ulemerero. Inu simukanakhoza kumupatsa iye kalikonse koma maenje a matope.”

⁴⁹ Koma mayi wokalamba wa tsitsi la imvi anati, “Koma ine ndinampatsa iye moyo.” Izo zikupangitsa kusiyana. “Ine ndinamupatsa iye moyo.” Ndipo Mulungu anamupatsa iye Moyo Wamuyaya. Zoon chotani, mayi!

⁵⁰ Nthawi zina anthu amanena kwa ine, makamaka kawirikawiri mu misonkhano yanga, ine “mowirikiza kulalikira za chiwukitsiro.” Ndipo ine ndinawerenga kachigawo mmawa

uno, mutu wa 15 ndi ndime 4 ya Akorinto Woyamba, pa chiwukitsiro.

⁵¹ Koma, inu mukuwona, momwe iwo amamuyikira mayi lero, ndiwo mphika wa maluwa utakhala pafupi ndi mayi wokalamba, amene ali wokalamba ndipo sangathe kudzuka, mwina, ndi wofooka, ndi wa mutu wa imvi, ndi makwinya, ndipo atakhala mu mpando wa ndalema. Izo nzoona mokwana. Koma ine ndikufuna kutenga mfundo yanga ndi kukujambulirani inu chithunzi china cha chomwe mayi ali.

⁵² Winawake anati, “Inu mumalalika kwambiri za chiwukitsiro. Kwambiri Uthenga uliwonse uli ndi chinachake cha za chiwukitsiro.”

⁵³ Bwanji, ndithu. Ndi ujeni—ndi malo opumira ofunika a Uthenga. Ngakhale Iye anachita chiyani, ngati Iye sanawukenso kwa akufa, ndiye zonse izo zinali zopanda pake. Izo, kwa ine, zikutsimikizira kuti Iye anali Mulungu. Zikutsimikizira chirichonse Iye anadzinenera; chiwukitsiro! Ndipo awonso ali malo opumulirapo a moyo. Apo ndi pamalo poyambira. Apo ndi pachimake pa chithonθοzo chathu.

⁵⁴ Ndipo pamene ife tikuwona kuti Iye anawuka kwa akufa, izo zimatiyika ife, ndi zida za Uthenga, kutsogolo kwa nkondo, kukatenga malo, kukamenya. Pakuti, ife tikudziwa Iye anati, “Iye amene adzataya moyo wake chifukwa cha Ine adzawupeza iwo kachiwiri.”

⁵⁵ Ndipo ine ndikuganiza kuti ndi chimake chachikulu cha a Uthenga Wathunthu, ndicho chiwukitsiro, ndipo malonjezo ake Auzimu, ndi chithonθοzo chomwe icho chimapereka kwa iwo amene akudalira mwa icho. Pakuti, icho chimalonjeza chilumikizo chopambana cha kulumikizana kwathu limodzi kachiwiri. Icho chimalonjeza, ndipo ku—kuzirala kwa machimo onse. Icho chimalonjeza kuzirala kwa kulumala konse, kuvutika konse komwe ife tachita mmenemu, tinayenera kupyola nazo, mu moyo uno. Icho chimalonjeza, ndipo kusapezeka kwa zake zonse. Icho chimalonjeza kuti ngakhale imfa idzataya kufumbata kwake, ndipo ife tidzawuka mofanana ndi Yesu. Koteru, mwa malingaliro anga, chiwukitsiro ndicho chopambana cha malonjezo onse mu zinthu za Malemba. Apo ndi pamene icho chinasingidikiza.

⁵⁶ Ndipo nthawi ya Chiwukitsiro yapitayi, pamene ine ndimalalikira pa zinthu zisanu za:

Wamoyo, Iye anandikonda ine; kufa, Iye anandipulumutsa ine;
 Kuyikidwa, Iye ananyamulira machimo anga kutalitali;
 Koma, kuwuka, Iye analungamitsa mwaulere kwa nthawi zosatha.

57 Ilo ndi Tsiku la ine, Tsiku lopambana la masiku! Ndipo kuwona chimene ilo liti lidzatanthawuze, kwa ife tonse, mu chiwukitsiro, pamene ife tikukangalika ndi kuyembekezera Tsiku la masiku lodalalo!

58 Icho chimatipatsa ife lonjezo kuti tsiku lina kuti awa okalamba, otha mphamvu, ofooka, a mutu wa imvi, azimayi owerama adzasinthika. Osati kuti amayi adzangokhala pamene, pa okha, koma onse a mu banja lawo palimdozi nawo.

59 Ndipo ilo lidzakhala tsiku lotani! Idzakhala nthawi yotani, pamene ife tidzayang'ana pa nkhope za iwo amene ife tawakonda bwino kwambiri! Sikusiyana kwake mmawa umenewo, pamene ife tidzawone okondedwa athu, ndi—ndi kuyang'ana chimene iwo adzakhale! Zopweteka zonse zidzachotsedwa. Zowawa zosokoneza zonse zidzathedwa. Kulibenso masaya otumbululuka a imfa. Kulibenso misozi yochokera mmaso. Malonjezo a chiwukitsiro onse a izi. Uko sikudzakhalanso maliro. Kulibenso kuisita mwana pa tsaya, amene ali ngati kachidutswa ka mwala; kumene oyika maliro amalikonza thupi, ndi kulitukumula ndi kulipaka utoto, ndi zina zotero, kuti liziwoneka mwachilengedwe. Izo sizidzafunikanso, kumeneko.

60 Ndiye ine ndikuganiza za pamene ife tikuwawona iwo atayima kutsidyako, okondedwa athu, amayi athu, abale athu, anzathu onse; ndi kuwawona iwo mu matupi awo osavunda, matupi awo akumwamba; kuyang'ana khalidwe lawo, kuwona momwe iwo akudzichititsira ndi kukoma uko ndi chifatso, kulibenso manjenje kapena zokwiyitsa. Kuwawona iwo pamene atayima mofanana ndi Ambuye Yesu, limenelo lidzakhala tsiku lodabwitsa.

61 Ndipo aliyense wa ife, mu malingaliro athu, ali woyembekezera ndi kukhumba ora limenelo la chitonthozo, pamene ife tikukumana nawo. Aliyense akuganizira za wokondedwa wawo, mwina mayi wawo amene watsogola kale. Ndipo ilo lidzakhala tsiku lotani, pamene inu mukuwawonanso iwo! Ndipo kwa bambo, ndi kwa m'bale, ndi kwa . . . onse amene ali okondedwa, ilo lidzakhala tsiku lotani!

62 Ine ndikuganiza, nanenso, pakali pano. Ine ndikuganiza za banja langa, chomwe ilo lidzatanthawuze kwa ine pa Tsiku limenelo.

63 Ine ndikuganiza kuti, mmawa wa chiwukitsiro umenewo, mwina woyamba adzabwera kudzakumana nane adzakhala mwana wanga Sharon. Ayi, iye sadzakhala akunjemera. Mdierekezi ameneyo sangalowe mu malo amenewo. Kulibe meningitis yomwe ingakhudze Dziko limenelo. Iye sadzandigwedezera dzanja kuti ndapita. Tija tating'ono, timaso ta buluu tidzakhala tikuvina pamene iye akuponya mikono

yake chotero nafuula, “Adadi!” Ine ndidzakhala wokondwa kumuwona iye, kudziwa kuti iye sadzakhozanso kufa; kudziwa kuti zonse zatha, chifukwa chomwe ine ndinalalikira chiwukitsiro molimba kwambiri.

⁶⁴ Ndiye ine ndidzawona mayi wake, mayi wake wa Billy, mnyamata wanga. Ndipo ine ndiri ndi zokumbukira zambiri pomwepa zimene zikukhalapobe. Ine ndikukumbukira pamene ine ndinali kumutenga iye; kapena Bambo Combs, apa kuno, anali kumutenga iye kukamukweza kotsiriza, ndipo ine ndinali kumutsatira iye, mu galimoto. Pamene ife tinapita kumusi uko ku Seventh Street, komweko; Billy, ali wa miyezi khumi ndi isanu ndi itatu.

⁶⁵ Momwe iwo amakhoza kubwera naye ku msewu, ndi kumulola iye kuti amuwone. Ndipo iye amakhoza kugona namalira, ndi kuyang’ana pa mwana wake, koma samakhoza kufika moyandikira kwa iye.

⁶⁶ Ndiyeno popita ku msewuko, oyika maliro anabwera napita ku—ku—ku Seventh Street. Mayi awa anali akumusamalira iye pa nthawiyo. Ndipo iye anali atayima kunja pabwalo, atavala kakabudula kakang’ono, ndi ka kapusi kofiira atakakokera cha m’mbali pa mutu wake. Ndipo pamene mayi wakeyo, atagona pa machira aja, m’mbuyo mwa ambulasiyo, akundipenyetsa ine, pamene iye amamuwona mwana wake atayima mu bwalo, kudziwa kuti iye akukakwera kotsiriza; iye anadzuka pa machira nafuula, ndi kutambasula manja ake owonda, kuti amukumbatire mwana wake mu bwalo. Koma sakanakhoza kumutenga iye.

⁶⁷ O, chidzakhala chimwemwe kumuwona iye tsiku limenelo. Ayi, iye sadzakhala ndi manja owonda, ngakhalenso masaya ake sadzalowa mkati. Koma iye adzayima mwa kukongola kwa mmwamba kwa mfumukazi ya Kumwamba, ndi kwa mayi. Maso ake akuda, akuda ngati mapiko a khwangwala, adzakhala akuvina ndi chimwemwe. Iye sadzakhala wowelama konse; pomwe, Mdierkezi uyo wa TB sadzalowanso mu Dziko limenelo. Koma, opanda chivundi, adzayima mwa kufanana ndi Iye.

⁶⁸ Ine ndikuyerekeza, ndiye, wosatira kudzakomana nane adzakhala Edward, amene ife tinkamutcha “Humpy,” mwa dzina lachidule. Iye anali woyamba pa kulumikizana kusanu ndi kunayi kwa unyolo, unyolo wa banja la a Branham. Iye anali mfundo yoyamba kuduka; amene anandiponda ine. Ine ndidzamuona Edward akubwera chothamanga kwa ine. Komabe, iye anamwalira ali mnyamata, wa zaka khumi ndi zisanu ndi zinayi. Ndipo pamene ine ndidzamugwira iye dzanja lake, ine ndikutsimikiza ife tidzakhala ndi zinthu zambiri zoti tikambirane, za chinyamata, chifukwa ife tinali okondana. Ife timamatirana limodzi. Iye amandirola ine kuvala suti yake, ndi—

ndi—ndi zinthu, monga abale enieni amachitira. Chidzakhala chokondweretsa kumuwonanso iye.

⁶⁹ Ndipo ine ndidzamumva iye akunena chinachake chotere, “Kodi iwe unamva mawu anga, Billy? Iwe unali ukugwira ntchito koweta ng’ombe, pa nthawi ya kuchoka kwanga kwa pa dziko. Koma mu chipatala, ine ndinatuziza mawu, ‘Kamuuzeni Bill zonse ziri bwino.’”

Ine ndidzakhala wokondwa kuti, “Inde, ine ndinalandira mawu ako, kuja ku dambo.”

⁷⁰ Ndiye, ine ndimayerekeza, motsatira adzabwera bamba anga. Iwo anali mfundo yotsatira kuduka, ndipo. . . Ayi.

⁷¹ Ine ndikuganiza Charles anali mfundo yotsatira, mng’ono wanga wina. Iye anachita ngozi ya galimoto pamene anali mnyamata wamng’ono chabe. Iye nthawi zonse anakokoka mwendo wake wakumanja, pamene iye ankayenda. Koma, inu mukudziwa, pamene ine ndidzamuwona iye, iye sadzakhala akukokanso mwendo umenewo. Zimenezo zidzakhala titasiyana nazo, adzayima mwa kukongola kwa mnyamata wamng’ono.

⁷² Ndipo iye adzanena kwa ine, chinachake monga ichi, pamene iye akumwetulira. Iye adzati, “Inde, Bill, kulibe ngozi kumwamba kuno. Ndipo ine ndikukumbukira usiku uja ine ndisanatengedwe mu ngozi ya galimoto, iwe unalankhula kwa ine, utayima mu mpita wa mu kanyumba kathu kosawuka,” ndipo ine ndikuyang’ana pa mwamba pake, tsopano lino. “Iwe unalankhula kwa ine za Ambuye, maora ochepa ndisanachoke. Ndipo iwe unali pa gome ukulalikira pamene ine ndinkachoka.”

⁷³ Ndiye adzabwera adadi. O, ine ndidzawaona iwo. Ngakhale iwo anandipatsa ine zikwapu zowawa zambiri, zomwe ine ndinachita kuziputa, koma ine ndidzawona mulu wa tsitsi lakuda logwedezeka, lokongola kwambiri kuposa kale, pa tsiku limenelo. Ndipo iwo adzayang’ana pa ine, ndi kuti, “Mnyamata wanga, iwe ukudziwa, Adadi sadzayimirira kuchokanso pa tebulo kuno, ayinso, anjala, kulola ana ake kuti adye, pakuti kuno ife tiri nazo zambiri. Kulibe za kusowa kuno.”

⁷⁴ Kuwawona iwo pamene amakhoza kugwira ntchito, ndipo akulandira 50 cents kapena 75 cents pa tsiku, ndiyeno kumachoka pa tebulo kuti ana akhoze kudya, nkubwerera kukagwiranso ntchito. Ndipo iwo ankagwira ntchito molimbikira mpaka malaya awo amawawuka ndi dzuwa pa nsana pawo, ndipo mayi amangowadula ndi sizasi.

⁷⁵ Ine ndikukhoza kuwamva iwo akunena chinachake motere, “Bill, iwe ukukumbukira usiku uja iwe ndi M’bale George munabwera kudzandipempherera ine pamene ine ndinali kupita? Iwe ukudziwa, ine ndinawawuza mama kuti panali Angelo oyera awiri atayima pa kama, ndi mngelo wofiira ku mapazi. Ndipo mngelo wofiirayo amayetsa kunditenga

ine, koma Mngelo woyera anayima pakati. Iwo potsiriza ananditengera ine Kwathu.”

⁷⁶ Ndiye, winanso, wotsatira kupita mu mfundozo, kapena amene anapita, adzabwera Howard. Ine ndidzamuwona Howard; monga ife tinkakonderana limodzi kupita ku mayiko, kulikonse; woyitanidwa kudzakhala mtumiki; umunthu wopambana, koma oyanjana nawo ankamubwezera iye mmbuyo. Kulankhulana kotsiriza kumene ine ndinali nako ndi iye, iye anati, “Pamene ine ndipita, Bill . . .”

⁷⁷ Ine—ine ndinamuwona iye akupita, mwa masomphenya, pafupi zaka zinayi iye asanapite. Ndinamuwuza iye kuti ine ndinawona Pop akulemba manda ake nati amenewo anali otsatira ake.

⁷⁸ Ndipo iye anati, “Pali chinthu chimodzi ine ndikufuna iwe undichitire ine.” Iye anati, “Ine ndayipitsa moyo wanga. Ine ndakhala ndikungokwatira ndi chirichonse. Ine—ine sindikudziwa chimene chachitika.”

Ine ndinati, “Kodi ukumukhulupirira Iye, Howard?”

⁷⁹ Iye anati, “Ndi zonse zimene ziri mwa ine, ine ndimamukhulupirira Iye.” Mwa pafupi masiku awiri kapena atatu iye asanachoke, iye anapanga mtendere wake ndi Mulungu, limodzi ndi M’bale Neville ndi ena pamenepo. Ndipo iye anati, “Pali chinthu chimodzi ine ndikufuna inu muchite. Pamene ine ndipita, Bill, udzawayimbitse kwa ine, *‘Iye Adzavetsa, Nati, ‘Wachita Bwino.’*”

⁸⁰ Ine ndikukhulupirira, ine ndisanagwirane chanza ndi Howard, ine ndidzamumva iye akuyima nayang’ana pa ine, nati, Bill, Iye anamvetsa.”

⁸¹ Zitatha zimenezo, kudzabwera M’bale Seward, M’bale Frank Broy, M’bale George DeArk. O, chiwukitsiro chikutanthawuza zambiri kwa ine. Ine ndikuyembekezera pa korona wopambana wa oralo. Ndipo pamene Kuwala kukuyamba kufalikira, “Ife tidzadziwa momwe tikudziwikira.” Ife tidzavetsa, ndipo—ndipo tidzakumbukira omwe tinkayanjana nawo ndi a—amene akhala ali kumeneko.

⁸² Ndipo—ndipo ambiri, kudzakhala ambiri kumeneko amene ife sitinkaganiza konse kuti adzakhhalapo uko. Pakuti, inu mukudziwa, ndi pa nthawi imeneyo, imene ine ndikukhulupirira kuti “mkate umene ife tawutayira pa anthu, madzi ovundulidwa, udzabwerera kwa ife pa Tsiku limenelo.” Pamene ife tikuwona zomwe umboni wathu unachita, pa anthu amene ife sitinawamvetse machitidwe awo kwa Icho, adzakhhalapo mwina kumeneko. Ndi Tsiku lotani lidzakhale limenelo!

⁸³ Ndiyeno, aponso, mbewu zomwe ife tinadzibzala, mosaganizira ngakhale kuti chimene iwo akanadzachita, koma kuno iwo alipo. Iwo anabala zipatso zofunika, ndipo ife

tidzawawona iwo pa Tsiku limenelo, okonededwa ena a mmbali ndi abale.

⁸⁴ Ndipo ine ndikuganiza za zikwi zimene ine ndaziwona zikutembenuka, inde, mpaka mamilioni tsopano, kupita, ndi chomwe utumiki wawo unali. O, zidzatengera choposa chiwukitsiro. Zidzatengera Muyaya, kupita mozungulira, kugwirana chanza ndi kupeza zinthu zimene ine sindikuzidziwa tsopano.

⁸⁵ Kumeneko kudzakhala amayi a mitu ya imvi, amene inu mukuwavalira maluwa oyera amenewo lero, amene adzakuwonani inu, ndipo iwo adzakhala okongola. Osati kuyimiridwa ndi mphika wa maluwa, kapena chithunzi china cha munthu wokalamba wa mutu wa imvi; koma mwa kufanana ndi kukongola kwa chiwukitsiro, iwo adzayima mofanana ndi Khristu, matupi awo akumwamba, aang'ono ndi okongola kosatha. Zedi, uwo ndiwo mpumulo. Ilo ndilo Tsiku la anakubala limene ine ndikuyembekezera. Uko ndiko kuvala korona. Osati duwa la pa chigube, koma kuvala korona kwa moyo, pakuti Mulungu wamusintha iye!

⁸⁶ Ine ndikuganizira za mayi anga okalamba, okalamba ndi ofooka, ndipo akugwedezeka ndi manjenje. Iwo sadzamachita zimenezo Tsiku limenelo. Zidzakhala zosiyana pamenepo. Ndipo Kuwala kwakukulu kukuyamba kufalikira, pamene ife tikuyamba kuyang'ana pozungulira, ndipo bwalo lalikulu lidzakhala likukulira ndi kukulira ndi kukulira. Izo zonse zikungowonetsera kuyandikira kwa Yesu. “Ndipo patapita kanthawi,” monga nyimbo inanena, “ndipo ine ndidzamuwona Yesu potsiriza.”

Iye adzakhala akundiyebekezera ine,
 Yesu wachifundo kwambiri ndi woona,
 Pa Mpando Wake wachifumu wokongola, Iye
 adzandirandira ine Kwathu
 Tsiku ili litapyola kale.

⁸⁷ Ndiye pamene ife tikumuwona Iye, ndipo ife sitidzakhala monga momwe tiliri tsopano. Ife tidza—tidzadziwa momwe tingamukondere Iye kwambiri. Ife sitidzayima kumbuyo ndi mantha pang'ono; chifukwa, ife tidzafanana Naye. Chabwino, Iye adzakhala woposa m'bale kwa ife koposa momwe Iye aliri tsopano. Ife tidzamumvetsa Iye bwino. Chifukwa, ife tiri kutali kwambiri, mu matupi achivundi; apo ife tidzakhala ndi thupi monga thupi Lake laulemerero. Ife tidzadziwa momwe tingamupembezere Iye. Ndipo pamene ife tikuwona chomwe Kukhalapo kwa Thunthu Lake kwachita kwa ife, kutisintha ife; wokalamba kukhalanso wamng'ono, onse opunduka kuwongoledwa. O! Ife tidzamvetsa pamenepo chifukwa chimene kumphamvu Yake inatichiritsa ife.

⁸⁸ Mafunso amene akhala mu malingaliro athu, “Iye angachichite motani ichi? *Ichi* chingachite chiyani?” Mwinamwake, mwachinsinsi, iwo onse adzatheratu. Mfundo zimene zamangidwa kumbuyo kwa malingaliro athu, “Kodi zidzakhala izi? Zingadzakhale motani izo?” Mwinamwake, kapena wina, zala zaufumu zidzangochotsa zomangirizika, kumasula mfundo zimenezo, ndipo izo zonse zidzaziralira mu korona mmodzi wamkulu wa chikondi.

⁸⁹ Ndiye ife tidzamuwona Iye. Ndiye ife tidzafanana Naye. Ndiye ife tidzamupembedza Iye. Ndiye ife tidzawona mayi momwe Mulungu amawafunira iwo.

Mayi sakanakhala wokwanira Kumeneko popanda banja lake.

⁹⁰ Poti, nthawi yopambana ya moyo wake wonse ndi kuwona ana atazungulira tebulo, ndipo onse a iwo ali athanzi ndi okondwa; ndi—ndi—ndi kuwona iye akuthira khofii, kapena chirichonse chomwe iye amachita, nakonza chakudya cha madzulo, ndipo iye ndi adadi atakhala pansi. Bwanji, imeneyo ndiyo nthawi yokondwetsetsa mu moyo wa mami, kuwona ana ake onse ali kunyumba.

⁹¹ Tsopano, musaphonye, musadzakhale mukusowa Tsiku limenelo. Lolani unyolo wopambana wa banja lanu ukhale wolumikizana limodzi, mfundo ndi mfundo. Lolani sipoko iliyonse ikhale mu gudumu. Ndiye pamene ife tikhala pansi ndi mabanja athu ndi magulu, ponseponse ku madenga a Muyaya, lidzakhala Tsiku lotani limenelo! Ndiye ife tidzamvetisa.

⁹² Anali Iye amene analonjeza ichi, mu Chivumbulutso 1, pamene Anati, kuti, “Lupanga lakuthwa konse-konse linatuluka mkamwa Mwake.” “Iye anali kitchedwa Mawu a Mulungu.” Ndipo zinali kuchokera mu milomo yomweyo, kuti anati, “Ine ndine Iye amene ali moyo, amene anali wakufa; ndipo Ine ndiri wamoyo kosatha.” Kuchokera mu milomo yomweyo, mu Yohane Woyera 6, makumi atatu-...akunena ichi, kuti, “Ine sindidzataya kanthu, koma Ine ndidzaliwukitsanso ilo mu masiku otsiriza.” Anali Iye amene anapanga lonjezo; milomo yofunika yomweyo. Iye ali Mmodzi Amene amatipulumutsa ife, Amene amatichiza ife, Amene anatiwombola ife, ndi Amene adzatiwukitsa ife pa tsiku lotsirizalo.

⁹³ Ngati inu muli mfundo yaing’ono yofooka imene yalekanitsa chilumikizano chachikulu cha banja ichi pa Tsiku limenelo, Mulungu wa Kumwamba, mmawa uno, mwinamwake mwa njira yachinsinsi, amasule mfundo zazing’ono izi zimene zamangidwa mu malingaliro anu, ndi kuwulula kwa inu chikondi chimene Iye ali nacho kwa inu, ndipo mukhoze inu kubwera mokoma kudzamutumikira Iye.

Pamene ife tikuganiza za zinthu izi, tiyeni tipemphere.

⁹⁴ Ife tisanapemphere kumene, ndipo inu muweramitse mitu yanu, ine ndikufunsani inu. Kodi inu mungakonde kuti, pa Tsiku ili La Anakubala, kuti muyiperekenso miyoyo yanu mwatsopano kwa Iye, kuyang'anira mtsogolo ku chiwukitsiro chimenecho? Kodi mungakweze manja anu kwa Iye? Pamene aliyense... Mulungu akudalitseni inu.

⁹⁵ Kodi pangakhale wochimwa amene ali pano tsopano, akhoza kunena, "O Mulungu, ine sindinadzilumikize nawo mu mfundo imeneyo. Ine ndine wosowayo amene sadzakhalapo kumeneko pamene mayi akumka namakayang'ana ponseponse mu Ulemerero. Ine sindidzakhalapo kumeneko, pakuti ine sindinapange kose mtendere wanga ndi Mulungu. Ine ndiribe chiyembekezero cha Moyo Wamuyaya mwa ine. Koma lero ine—ine ndikufuna kuchita zimenezo?" Kodi mungakweze dzanja lanu, kunena, "Mundipempherere ine, M'bale Branham, pa nthawi iyi. Ine ndikufuna kukumbukiridwa mu pemphero, pakuti ine ndiri nawo okonedwa patsidya la nyanja, nyanja ya Moyo, ndipo ine ndikufuna kukakumana nawo?" Kwezani manja anu.

⁹⁶ Kapena winawake amene wabwerera mmbuyo, ndipo akufuna kubweranso pa tsiku ili, ndi kuti, "Ambuye, ine ndikudziperekanso ndekha kachiwiri kwa Inu; kubwera kudzakonzanso pangano langa ndi Inu," kodi inu mungakweze manja anu?

⁹⁷ Atate athu Akumwamba, monga zikuyandikira, tsiku ili lidzapanga tsiku limodzi kuyandikira ku zochitika zopambanazo. Ndipo ife tachita kungokakamizidwa, chaka chirichonse, kuti tiwone ichi chikuyimiridwa.

⁹⁸ Monga anthu anazolowera kupita ku Yerusalemu pa Tsiku la Pentekoste, ndipo mwa kuyeretsa kwa kachisi ndi linga, ndi—ndi kupereka kwa nsembe ya tchimo; chaka chirichonse iwo amakumbutsidwa, pamene mwanawankhosa amafa kunja kuja, kuti kudzabwera nthawi yakuti Mwanawankhosa wa Mulungu akanadzafa, kulekana nalo tchimo. Nthawi iliyonse kamwanako kankaphipha, ndipo magazi mkumamwazikira mmanja awo, iwo anakumbutsidwa kuti kudzakhala nthawi pamene adzakhalapo Mwanawankhosa wa Mulungu, amene angadzafuule, "Eli, lama . . . ? Eli, lama . . . ?" pa mtanda.

Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti monga ife tikuyang'ana lero ndi kuwona zimenezo . . .

⁹⁹ Milungu ingapo yapitayi, ndisanachoke mu msonkhano Wanu, wa ku California, Indiana uyu anagona wopanda kanthu ndi wakufa, ndipo kunalibe moyo, kukhala ngati. Maluwa amene anafa nyengo yolakatitsa masamba yapitayo. Masamba analakatika mu mitengo. Ndipo zakudya zamitengo zinali zitapita ku mizu, ndipo chirichonse chinali chakufa.

¹⁰⁰ Koma kunali nyengo pamene dzuwa linayamba kuwala mwa njira yosiyana. Dzuwa lomwelo limene linali likuwala kupyola mu dzinja, koma mphamvu zinasintha ndipo linawala mosiyana. Ndipo mwa kuwala kwa dzuwa, palimodzi ndi mphamvu, moyo unatulukiranso, paliponse. Masamba kubwereranso ku mitengo. Masamba... Moyo umene unasiya tsamba, ndipo tsamba linathothokapo, koma moyowo unapita mu nthaka; iwo unabweranso mwa kukongola kwatsopano, mwa ubwino wa unyamata. Duwa lomwe linasiya zake—kununkhira kwake, limene linasiya kukongola kwake kowala niligwera mu nthaka; kubadwa, kutulukira kachiwiri mu unyamata wake, ndi kununkhira kwatsopano.

Kodi ife tikukumbutsidwa za chiyani, Ambuye, pa maora awa?

¹⁰¹ Ndipo dziko kusandulika kuchokera mwa chipululu chosawala, cholira, kukhala paradizo wa kukongola, ndipo njuchi ndi mbalame kunayimba, ndi chirichonse mwa mtima-wopepuka, ndipo mitengo ku—kunyadira mu mphepo za kachiyeziyezi kofunda ka nyengo ya kuphukira. Kufunda ndi chimwemwe zinali padziko kachiwiri, chifukwa cha dzuwa, s-u-n.

¹⁰² Koma tsiku lina S-o-n akudza ndi machiritso mu mapiko Ake, ndipo miyoyo yaing'ono iyo yomwe yabisika monga zakudya za mu mitengo, mu nthaka, monga mo—moyo womwe uli mbewu ya duwa, iye adzaubweretsa iwo mwatsopanonso, osadzaziralanso. O, momwe ife tikukuthokozerani Inu pa ichi!

¹⁰³ Ndipo panali ambiri, manja ambiri amene anakwera mmwamba mmawa uno, pakuti iwo akudziwa kuti kuseri kwa chophimba uko, kuli chinachake. Iwo akukhumba kudzawaona mayi. Iwo akukhumba kudzawaona okonedwa awo ndi oyanjana nawo, ndi kudzazindikira zinsinsi zonsezi, momwe iwo anadzera kuno, ndi kupyola mu nthawi. Zonse zagona kuseri kwa chophimba chobisika. Ndipo tsiku lina Inu mukubwera. Ndipo iwo anakweza manja awo; iwo—iwo—iwo—iwo akufuna kutsimikiza, Ambuye. Iwo akudzikonza okha kachiwiri, ndiponso ine ndikutero. Tsopano tithandizeni ife, Ambuye. Konzaninso chikhulupiriro chathu ndi mphamvu zathu.

¹⁰⁴ Ndipo pamene ife tikumverera kuyandikira kwa Ambuye. Ndipo zaka makumi anayi zapitazo, kunafalikira pentekoste watsopano panso pano. Mzimu kuyamba kuwulula zinthu. Ndipo pano ife tiri pa chizindikiro chotsiriza, kusanafike kumene Kudzako. Ife tikudziwa kuyandikira kwa Ambuye kwafupikira. Ndipo ife tikuwona odwala akupangidwa kukhala bwino kuchokera ku matenda awo, chimene chakhala cha chinsinsi kwa dziko, kwa zaka zikwi ziwiri, chichokere atumwi. Koma pano izo zikuwonekeranso, aneneri akuwuka, Angelo

akuwonekera, zizindikiro ndi zozizwitsa. Ndi chiyani icho? Chiwukitsiro chikuyandikira pafupi. M-w-a-n-a akubwera.

¹⁰⁵ Tiroleni ife tikhale okonzeka, Ambuye. Tiroleni tikumbatire lonjezo Lauzimu lirilonse; musaganizire mfundo zazing’ono izi zimene zakundikidwa ndi sayansi, ndi zina zotero, kuti izi sizingachitike. Lekani izo ziyambe kumasuka, mmawa uno, mopanda chivundi...[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]...pamene Iye akumveketsa Mawu a Baibulo la Mulungu, monga choyimbira chochunidwa bwino, kuti chiyimbe nthetemya, “Ine ndine Iye amene anali wakufa, ndipo ali wamoyo kwa nthawi zochuluka.” “Kanthawi kochepe, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine.” “Pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka mapeto a dziko.” “Ndipo zidzachitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, kuti Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa matupi onse; zizindikiro ndi zozizwitsa; akulu adzalota maloto, ndipo anyamata adzawona masomphenya,” chizindikiro cha mvula ya masika ndi nthawi yotsiriza. Iloleni iyo tiimverere pakati pathu, mmawa uno, Ambuye, ndipo chikhulupiriro chathu chitakhala chotetezedwa. Pakuti tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.



TSIKU LA ANAKUBALA CHA59-0510M
(Mother's Day)

Uthenga uwu wa M'bale William Marriion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, pa 10 Mei, 1959, ku Branham Tabernacle, ku Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1992 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org